

# Banja laling'ono, umoyo wathanzi mboma la Karonga

Banja la anthu ochepta limapindula mokwanila kuchokela ku zithandizo zosiyanasiyana za mdziko zokhudza miyoyo yavo.

- Mu zaka makumi awiri zapitazi chiwerengero cha anthu mu mzinda wa Karonga chachulukitsidwa kulira pa  $\frac{3}{4}$  kuchoka pa anthu 44 kufika pa anthu 80 pa km<sup>2</sup> ili yonse.
- Nyumba zokhala anthu asanu ndi mmodzi (6) mwa nyumba zianu ndi ziwiri (7) zili zones zili ndi potunga madzi a ukhondo pa makono.



**Nyumba zokhala anthu zisanu ndi zinayi (9) mwa nyumba khumi (10) zili zonse zimagwilitsa ntchito nkhuni pophika; ndipo nyumba imodzi (1) yokha mwa nyumba khumi ndi anayi (14) zili ndi magetsi.**

**Amayi amodzi (1) okha mwa amayi makumi awiri (20) aliwонse; komanso abambo amodzi (1) mwa azibambo khumi (10) aliwонse ndi amene amamaliza maphunziro awo a ku sekondale.**

- Amayi atatu (3) mwa amayi anayi (4) aliwонse komanso abambo anayi (4) mwa abambo asanu (5) aliwонse amadziwa kulemba, kuwelenga ndi kuwelengera.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwонse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo makumi awiri (20) aliwонse sali pa ntchito iliyonse yolembedwa.
- Amayi atatu (3) mwa amayi ananu ndi awiri (7) aliwонse amavutika kwambiri kupeza chithandizo cha mankhwala akad wala chifukwa zipatala zoyandikila ndi kumene amakhala zili kutali kwambiri.

## Ubwino wotsatira njira za kulera

Banja likakhala ndi ana ochepta, zimathandiza makolo a anawa kuwaphunzitsa mokwanila ana awo ndipo chifukwa choti aphanzira bwino, anawa amakhala ndi mwayi wopeza ntchito zabwino mtsogolo. Kuchepetsa kachulukidwe ka anthu mdziko kumathandiza boma ndi mabungwe othandiza boma kukonzekera bwino pa ntchito zopititsa umoyo wa anthu patsogolo monga kukhala ndi madzi a ukhondo, ntchito za umoyo komanso za mtengatenga.

## Banja la anthu ochepta limakhala ndi mayi wa moyo wathanzi komanso banjalo limakhala losangalala



**Amayi amabeleka ana asanu ndi mmodzi (6) pa moyo wao wonse koma amaonetsa chidwi chobeleka ana anayi (4) kapena asanu (5) wokha pa moyo wao wonse.**

**Amayi awiri (2) mwa amayi asanu (5) aliwонse a zaka za pakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zinayi (19) ayamba kale kubeleka ana.**

- Amayi amodzi (1) mwa amayi atatu (3) aliwонse amabeleka kunyumba osati kuchipatala.
- Amayi anayi (4) mwa amayi asanu ndi awiri (7) aliwонse omwe ali pa banja amatsata njira za kulera; ndipo amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwонse amatsa njira zolererazi kuti asabeleka ana ambiri.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu (5) aliwонse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo anayi (4) aliwонse amakhulupilira kuti ndi zovomelezeka kuti mamuna akhoza kumenya mkazi wake nthawi zina.

## Ubwino wotsatira njira za kulera

Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwонse a zaka zapakati pa khumi ndi zasanu (15) ndi makumi anayi ndi zisanu ndi zinayi (49) amamwalira pa nthawi yobeleka mwana. Kutsatila njira za kulera kumathandiza amayi omwe ndi achichepeleko kutenga nthawi asanakhale ndi mimba (pathupi) ndipo kutenga nthaw chonchi kumathandiza kuti asapeze mavuto mthupi mwawo omwe amadza chifukwa chobeleka akadali ang'ono. Amayi ngati akhala ndi ufulu wosankha nthawi yoti abeleke komanso kusyanitsa zaka za ana obelekedwa zimawathandiza kuti akhale ndi moyo wathanzi. Ana omwe amayi awo anamwalira nthawi zambiri samamaliza maphunziro awo ku sukulu.

## Banja la anthu ochepta ana ake amakula bwino komanso amakhala ndi moyo wathanzi

- Mwana mmodzi (1) mwa ana khumi (10) aliwонse wochepera zaka zisanu (5) amakhala ndi thupi lopelewela losagwilizana ndi msinkhu wawo.



**Ana awiri (2) mwa ana asanu (5) aliwонse wochepera zaka zisanu (5) amakhala wopinimbira.**

## Ubwino wotsatira njira za kulera


Kutsatila njira za kulera kumathandiza ma banja kuti ana awo akule ndi moyo wathanzi komanso kutha kuonetsetsa kuti pakupita nthawi yokwanila bwino pamene mwana wabadwa ndi nthawi yomwe mwana wina akudzabadwano mbanjamo. Ana obadwa mosiyana ndi zaka zitatu kapena kupitilira apo amakhala ndi mwayi wokhala moyo wochuluka kwambiri kuposa ana omwe abadwa mosiyana ndi zaka ziwiri kapena kuchepela apo. Makolo omwe ali ndi ana ochepta amasamalira bwino ana awo ndi kuwapatsa zakudya zokwanila.

Anthu awiri mwa anthu atatu aliwонse mbomali ali ndi zaka zosapitilira makumi awiri ndi zisanu (25)

Zaka

80+  
75-79  
70-74  
65-69  
60-64  
55-59  
50-54  
45-49  
40-44  
35-39  
30-34  
25-29  
20-24  
15-19  
10-14  
5-9  
0-4

Amuna Akazi



Source: National Statistical Office of Malawi, Population Projections Malawi.



**Mdziko la Malawi, amayi amodzi amamwalira pobeleka ana pa ma ola awiri aliwонse.**



**Mwana wakhanda mmodzi (1) wosakwana chaka chimodzi amamwalira ma ola khumi ndi awiri (12).**



**Pa ma ola asanu ndi atatu (8) alionse mwana mmodzi wosakwanitsa zaka zisanu amamwalira.**